# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

## ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA THYOLO M'DZINJA LA 2024-2025

## DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE


Nyengo ya dzinja ya 2024/2025 ikuyembekezeka kukhudzidwa ndi La Nina wochepa mphamvu. La Nina ndi kuzizira kwa madzi mdera la pakati chakum'mawa kwa nyanja yamchere ya Pacific. Izi zikhala chomwechi mpaka kumayambiriro a chaka cha 2025.
Boma la Thyolo likuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo wokhazikika, komanso oposera apo mu nyengo ya mvula ya 2024/2025.

## October 2024





Mweziwu, Madera ambiri kudzakhala kopanda mvula.
Komabe pali kuthekera kodzakhala ndi mvula ya Chizimalupysa yomwe idzakhale ya mphepo ndi ya mkuntho m'madera ena.

## November 2024





Nyengo yotentha ikuyembekezereka mwezi wa November 2024. Madera ambiri akhoza kulandira Mvula ya mlingo wa pakati pa 50-100mm yomwe idzakhale ya mphepo ndi ya mkuntho. Mvula yodzalira ikuyembekezereka kugwa kuyambira sabata lachitatu mpaka sabata lachinayi ya mwezi wa November 2024

## December 2024





Mu December, madera ambiri ali ndikthekera kolandira mvula ya mlingo okhadzikika kapena kuposera apo wa pakati pa 150-200mm. Madera ochepa a kwa TA Bvumbwe ndi SC Kwethemule akuyembekezereka kulandira mvula ya mlingo okwana 250mm

## January 2025





Mwezi wa January ukuyembekezereka kukhala wa chinyontho. Madera ambiri monga TA Chimaliro, Bvumbwe, Nsabwe, Kapichi ndi SC Mphuka
Akuyembekezereka kulandira mvula yoposa 300mm.

## February 2025





Mlingo wa mvula okhadzikika komanso oposera apo ukuyembekezereka kugwa mu mwezi wa February. Mvula ya mlingo wa pakati pa 150-250mm ikuyembekezereka kugwa madera ambiri

## March 2025




Madera ambiri akuyembekezereka kulandira mvula m'mweziwu koma mvula ya mlingo ochuluka ikuyembekezereka kugwa madera ena monga kwa TA Nchilamwela ndi SC Kwethemulo.


## April 2025




Madera ambiri ali ndikothekera kolandira mvula ya mlingo okhadzikika kapena ochera apo wa pakati pa 100mm ndi 150mm
Nyengo ya mvula ikuyembekezereka kufika kumapeto sabata lachiwiri mwezi wa April 2025.

*Mvula yodzalira ili ndi kuthekera kochedwerapo. Ndipo ikuyembekezereka kugwa kuyambira sabata lachitatu mpaka sabata lachinayi ya mwezi wa November 2024. Nyengo ya mvula ikuyembekezereka kufika kumapeto sabata lachiwiri mwezi wa April 2025. Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kukhala yotali masiku a pakati pa 120 ndi 150. Ng'amba yosapyola masabata awiri ikuyemnekezereka mwezi wa February 2025.*

| THYOLO | | |
|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 13.1 | 36.8 | 14.7 |
| NOV | 66.6 | 109.2 | 45.7 |
| DEC | 155.7 | 279.6 | 238.5 |
| JAN | 227.5 | 343.9 | 268.9 |
| FEB | 182.6 | 289.9 | 262.2 |
| MAR | 111.8 | 237 | 236.8 |
| APR | 46.8 | 95.2 | 92.6 |




**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**

**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw

Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku: